Chidziwitso: Utitiri wa Nkhuku

Utitiri umaoneka kawirikawiri pa nkhuku makamaka za kumudzi, muno m'Malawi.

Photo 2: Courtesy Back Yard Chickens ("casportpony")

Maonekedwe a Matendawa:

- Zizindikilo: Nthawi zambiri utitiri umawoneka ngati mzere wakuda pamwamba pa diso. Nthawi zina, umakhala paliponse pa mutu, kapena pena pa thupi la nkhuku. Umakhala wokhazikika pakhungu, osayendayenda.
- Umayamya magazi a nkhuku, ndipo nkhukuzo zimafooka. Zina zikhoza kufa koma zochepa.

Kuchiza:

- Pakani mafuta monga Vaseline pa utitiri. Zimenezi zidzawulepheretsa kupuma ndipo udzafa. Koma sudzagwa kwa masiku angapo. Izi zilibe kanthu.
- Thandizani nkhuku zonse zomwe zakhudzidwa makamaka zazikulu.
- Komanso thirani mankhwala monga Actellic kapena Akheri powder pansi mkati mwa khola. Chitaninso pakadutsa milungu itatu kapena inayi kuti muphe utitiri womwe wangotuluka kumene.

Kupewa:

- Musaiwale kuthira mankhwala pansi m'khola.
- Mphutsi za utitiri ziyenera kukumba m'nthaka kuti zibereke. Ngati sizingathe kukumba, sizingathe kubereka. Ngati pansi ndi simenti yolimba, utitiri sungathe kuberekana.
- Musabweretse nkhuku zomwe zili ndi utitiri m'khola lanu.

Copyright © 2013-2020 Rural Poultry Centre - All rights reserved
Copyright and linking policy «» Privacy policy «» Terms and conditions «» FAQ
Site last reviewed 30 December 2021